**F**oteleza wochita kupanga kuchokela ku mankhwala ali ndi **zotsatira zoyipa zobwera pa nthawi** yayitali pa chilengedwe chathu. Kawirikawiri:

- **amapha tizilombo tofunikila mu nthaka** – tizilombo tofunikilati ndi tating'onoting'ono, tamoyo timene timasintha zinyalala kukhala zinyatsi zodzala ndi michere yofunikila, imene ndi chakudya cha mbeu;
- **amathiridwa moposela muyeso** – izi zimachulukitsa mchere wa munthaka ndipo zimatentha mizu, kupangitsa zomela kuti zizikula mwa pang'onopang'ono, kusowa madzi, mapeto ake kufa kumene;
- **kuchulukitsa mchere wa nitrate munthaka** – zomela zobzyalidwa munthaka imeneyi ndi zowopsya kwa anthu;
- **amawononga kuthekela kwa kulekanalekana kwa nthaka** – ndi nthaka yokhayo yolekanalekana imene imatha kulola madzi alowelere;
- **amayendelela kupita ku makhwawa, mitsinje konanso m'nyanja**, kumene amakasokoneza chilengedwe cha m'madzi ndi kuwononga madzi;
- **amayendelela kupita ku madzi apansi pa nthaka komanso ku dothi la pansi** popanda kupeleka phindu lirilonse ku zomela;
- **amalimbikitsa madenda osiyanasiyana mu zomela;** komanso
- amapatsa zipatso ndi masamba okhala ndi **amapatsa zipatso ndi masamba okhala ndi**.




# ZOTSATILA ZA FOTELEZA WOCHITA KUPANGA KUCHOKELA KU MANKHWALA PA CHILENGEDWE

www.acbio.org.za info@acbio.org.za Tel +27 (0)11 486 1156

african centre for biodiversity